



Mwala

WANTENGO WAPATALI



Shaykh-e-Tariqat, Ameer-e-Ahl-e-Sunnat
Founder of Dawat-e-Islami, Allamah Maulana Abu Bilal

MUHAMMAD ILYAS

Attar Qadiri Razavi

مستشرق
الدين



آنمول ہیرے

Anmol Hiray

Mwala Wantengo Wapatali (Dayamondi)

Mawu awa analankhulidwa ndi Shaykh-e-Tarīqat Amīr-e-Ahl-e-Sunnat, muyambitsi wa Dawat-e-Islami ‘Allāmah Maulānā Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razavi دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَةِ mu Urdu. **Nthambi yomasulira** (Nthambi yomasulira) yamasulira mu Chichewa. Ngati mungapeze cholakwika chilichonse muKumasulira kapena kalembedwe, chonde ziwitsani nthambi yomasulira pa makeyala kapena keyala ya imelo ili m'musimu ndi chitsimikizo chofuna kupeza zabwino [Šawāb].

Translation Department (Dawat-e-Islami)

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

UAN: ☎ +92-21-111-25-26-92 – Ext. 1262

Email: ✉ translation@dawateislami.net

Mwala Wantengo Wapatali (Dayamondi)
Kumasulira kwa M'chichewa kwa 'Anmol Hiray'



Ma Umwini Onse ndi Otetezeka

Ufulu © 2025 Maktaba-tul-Madinah

Palibe gawo lililonse la bukuli lomwe likuloledwa kupangidwa, kapena kutulutsidwa, mwanjira iliyonse ngati, pa magetsi, zinthu zina, kupanga fotokope, kapena iliyonseyo, popanda chilolezo cholembidwa cha Maktaba-tul-Madinah.

Kutsindikiza koyamba: Zul-Qa'daĥ, 1446 AH – (May, 2025)

Wotsindikiza: Maktaba-tul-Madinah

Kuchuluka kwake: -

ISBN: 978-969-631-524-7

THANDIZO

Khalani omasuka kutipeza ife ngati mukufuna kuthandiza mu ntchito zotulusa mabuku kapena timabuku ting'ono ting'ono ta chipembezo ngati njira imodzi yopangira Isal-e-Sawab kwa okondedwa anu omwe anamwalira.

Maktaba-tul-Madinah

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah Mahallah Saudagran, Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

✉ **Email:** maktabaglobal@dawateislami.net – maktaba@dawateislami.net

☎ **Phone:** +92-21-34921389-93 – 34126999

💻 **Web:** www.dawateislami.net

الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ، وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى خَاتَمِ النَّبِيِّينَ،
أَمَّا بَعْدُ، فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ، بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ-

Pempho (Du'a) Lowerengera Buku

Werengani pemphero (Du'ā) lili m'mutsili musanawerenge buku kapena phunziro lililonse la Chisilamu, muzakumbukira chilichonse chomwe mwawerenga, إِنَّ شَاءَ اللَّهُ:

اللَّهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَانْشُرْ
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْإِكْرَامِ

Kumasulira

E inu Allah عَزَّوَجَلَّ! Titsekulireni makomo a kuzindikira komanso luntha, ndipo tichitireni chisoni! E inu amene muli Wolemekezeka komanso Wawulemerero!

(Al-Mustatraf, vol. 1, pp. 40)

Dziwani: Nfunireni zabwino Mtumiki (Ṣalāt-‘Alan-Nabī ﷺ) kamodzi kumayambiriro komanso kumapeto kwa Du'ā.

ZANKATIMU

Pempho (Du'a) Lowerengera Buku.....	iii
Mwala Wantengo Wapatali (Dayamondi)	1
Ubwino wa Şalât-‘Alan-Nabi ﷺ.....	1
Nthawi ya umoyo wathu komanso mwala (dayamondi) wantengo wapatali	3
Moyo ndi wawufupi.....	4
Kupitirira kwa kutuluka mpweya wopumira	4
Tsiku limalengeza... ..	5
Bambo kapena malemu!	5
Infā imabwera mozizimutsa	6
Kunong'oneza bondo ngakhale kwa okhala ku Mwamba!.....	7
Cholembela cha Nib	8
Zalani Mtengo mu Paradizo!.....	8
Ubwino wofunira zabwino Mtumiki (Şalât-‘Alan-Nabi ﷺ)	9
Kuposa zaka makumi asanu ndi chimodzi zopembeza	10
Zinthu zomwe tikuyenera kuchita zinthu zisanu zisanafike.....	11
Kukonderedwa kuwiri.....	11
Ubwino wa Chisilamu	12
Kufunikira kwa nthawi.....	13
Mawu a anthu amene anayigwiritsa bwino ntchito nthawi	13
Khazikitsani chizolowezi.....	16
Kupambana kwa m'mawa.....	17

zankatimu

Ngale 15 za luntha pogona komanso kudzuka	19
Tchati cha Kunvetsetsa Malemba	24

الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ، وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى خَاتَمِ النَّبِيِّينَ،
أَمَّا بَعْدُ، فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ، بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ-

MWALA WANTENGO WAPATALI (DAYAMONDI)

Ngakhale Satana atakupangitsani kunva ulesi chotani, yesetsani kuwerenga bukuli kuchokera kumayambiriro mpakana kumapeto. Muzapeza malipiro ochuluka mu umoyo uno komanso womwe uli nkuza, **إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ**.

Ubwino wa Ṣalāt-‘Alan-Nabī ﷺ

A’lā Ḥaḍrat, Imām-e-Aḥl-e-Sunnat Maulānā Shāḥ Imām Aḥmad Razā Khān رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ akufotokoza pa tsamba 122 la gawo 23 voluyomu ya Fatāwā Razawīyyah: Sayyidunā Abul Mawāḥib رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anati, ‘Ndinamuwona Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ku maloto. Rasūlullāḥ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati kwa ine, ‘Udzapatsidwa mwayi opemphera chikhululuko kwa anthu okwana chikwi ndi zana limodzi pa Tsiku Lachiweruzo.’ Ndinafunsa, ‘Yā Rasūlallāḥ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ! Zatheka motani kuti ndikhale ndi mwayi wotere?’ Rasūlullāḥ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, ‘Chifukwa Umandifunira zabwino (Ṣalāt) kwa ine mowirikiza.’

(Aṭ-Ṭabqāt-tul-Kubrā lish-Sha’rānī, pp. 101)

Ngati njira imodzi yofuna kutumiza zabwinozi, pangani chitsimikizo chopanga ubwinowu mu ntima mwanu powerenga

Salāt-‘Alan-Nabī, kapena, muzinena kumayambiro komanso kumapeto kowerenga Salāt-‘Alan-Nabī, lankhulani kuti, ‘Ndikutumiza zabwino (Salāt) ndiKuwerengayi kwa Rasūl Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ’.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Zinanenedwa kuti panali mfumu imene inali kudusa pafupi ndi munda wa zipatso ndipo iye ndi anthu ake anawona munthu wina akuponya miyala. Umodzi mwa miyalayi unafikira kugenda mfumu. Mfumuyi inalamura antchito ake kuti miyalayi ibweretsedwe pa maso pake. Antchito aja anamubweretsa munthu wosowekera mwamboyu kwa iye. Mfumu inafunsa, ‘Miyala yotereyi wayitenga kuti?’ Moyipidwa, iye anayankha ‘Ndayipeza pomwe ndimayenda pa malo abwinja aja, ndiye ndinayiyika nthumba langa. Pamene ndinafika pa Munda wa zipatso, ndinagwiritsa ntchito miyalayi kutcholera zipatso muntengo.’ Mfumu inafunsa modabwitsika, ‘Ukuziwa kufunikira kwa miyala imeneyi?’ Iye anayankha, ‘Ayi sindikudziwa.’ Mfumu inati, ‘Zidutsa za miyala imeneyi zinali miyala ya ntengo wapatali, ndipo ndinene kuti, mwala (dayamondi) wantengo wapatali omwe wangomuwononga kamba ka kusazindikira kwako.’ Pakunva izi, munthu wosowekera khalidweyu anazidzudzula ndikudandawula koma kudandawula kwake sikunali kopindulitsa popeza anali atatayidwa ndikuwonongeka mpaka kale kale.

Nthawi ya umoyo wathu komanso mwala (dayamondi) wantengo wapatali

Okondedwa abale achisilamu! Chimodzimodzi, nthawi ya umoyo wathu komanso mwala wantengo wapatali. Ngati tingayiwononge nthawi poyigwiritsa ntchito mu zinthu zosalungama, sitidzapeza ubwino uliwonse kupatula chiwonongeko komanso kudandawula mokukuta mano pa Tsiku Lachiweruzo.

Allah عَزَّوَجَلَّ analenga ndikutumiza anthu pano pa dziko la pansi ndi nthawi yoziwika kuti akwaniritse nfundo ndi zolinga zopatulika. Pa chifukwa ichi, zanenedwa mu Sūrah Al-Mu`minūn, Vesi 115, Gawo 18:

اَلْخَسِيْطُ اَنْتَ اَخْلَقْنٰكَ عَبْثًا وَّاَنْتُمْ اِلَيْنَا لَا تُرْجَعُوْنَ ﴿١١٥﴾

Sopano mukuganiza kuti tinangokulengani popanda cholinga komanso kuti kwa ifeyo simuzabwerera?

[Kanz-ul-Īmān (Kumasulira la Quran)] (Gawo 18, Al-Mu`minūn, Vesi 115)

Kutengera Vesi imeneyi, zalembedwa mu *Khazāin-ul-‘Irfān*: ‘Kodi simukulingalira kuti muzadzutsidwa Tsiku lachiweruzo ndikupatsidwa mphoto pa Tsiku lachiweruzo! Munalengedwa ndi cholinga chomupembeza namalenga zomwenso zili zokakamizika kwa inuyo. Pambuyo pobwerera kwa ife, muzapatsidwa mphoto pa ntchito zomwe munali kuchita.’

Kulongosola cholinga cha kulenga moyo komanso infa, zafotokozedwa mu Sūrah Al-Mulk, Vesi 2, gawo 29:

الَّذِي خَلَقَ الْمَوْتَ وَالْحَيَاةَ لِيَبْلُوَكُمْ أَيُّكُمْ أَحْسَنُ عَمَلًا ط

Yemwe analenga infa komanso moyo ndi cholinga choti muyesedwe kuti ndi ndani mwa inu angagwire ntchito zabwino.

[Kanz-ul-Īmān (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 29, Sūrah Al-Mulk, Vesi 2)

Moyo ndi wawufupi

Okondedwa abale achisilamu! Kupatula ma Vesi awiriwa, chifukwa cholenga anthu chatchulidwanso m'malo ena ochuluka mu Buku lolemekezeka la Quran. Munthu akuyenera kukhala pano pa dziko la pansi kwa nthawi yochepa. Mu umoyo wawufupiwu, iye akuyenera kukonzekera nthawi yayitali imene azakhale ali m'manda komanso Tsiku Lachiweruzo. Choncho, nthawi yomwe tili nayo panopayi ndi yantengo wapatali kothetetu. Nthawi ikutha. Siyingayimitsidwe kapenanso kukhala mu kulamulidwa kulikonse. Mpweya tikutulutsa ndi kulowetsawu tsiku lina suzabwereranso.

Kupitirira kwa kutuluka mpweya wopumira

Sayyidunā Ḥasan Baṣrī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ walankhula, 'Fulumirani! Fulumirani! Ndi cholinga chanji cha moyo wako – moyo wako ndi wozaza ndi kupuma mpweya. Ngati mpweya wopumirawo

Mwala Wantengo Wapatali (Dayamondi)

ungasiye, zinthu komanso ntchito zimene munthu angapeze chisangalalo cha Allah عَزَّوَجَلَّ zizasiyanso. Timupemphe Allah عَزَّوَجَلَّ kuti amunvere chisoni yense amene amalingalira za khalidwe komanso ntchito zake nagwetsa nsozi ndi chikumbu ntima poganizira machimo ake!’ Akulankhula kuti, iye رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anawerenga Vesi 84 ya Sūrah Maryam:

*Ife tikumaliza kuwerengera chiwerengero
chawo.*

إِنَّمَا نَعُدُّ لَهُمْ عَدًّا

[Kanz-ul-Īmān (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 16, Sūrah Maryam, Vesi 84)

Hujjat-ul-Islam Sayyidunā Imām Muhammad Bin Muhammad Ghazālī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anati, ‘Kuwerenga kukunenedwa apa ndi kopuma mpweya wawo.’ (*Iḥyā-ul-‘Ulūm*, vol. 4, pp. 205)

Tsiku limalengeza...

Sayyidunā Imām Bayḥaqī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ akufotokoza mu *Shu’ab-ul-Īmān*: Mtumiki wa Raḥmah صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, ‘Tsiku lililonse limalengeza pomwe dzuwa lukutuluka: ‘Ngati mukufuna kugwira ntchito yabwino komanso yolungama lero, gwirani chifukwa sindizabwereranso.’ (*Shu’ab-ul-Īmān*, vol. 3, pp. 386, Ḥadīṣ 3840)

Bambo kapena malemu!

Okondedwa abale achisilamu! Tikuyenera kugwira ntchito zabwino m'mene tingakwanisire kutengera mwayi wa tsiku

lililonse la moyo wathu infa isanatipeze nthawi ina iliyonse. Anthu amene akutitchula komanso kutiyitana ndi mayina komanso mifunda lero ‘bambo’ azakhala akutitchula komanso kutiyitanira dzina loti ‘malemu’. Tizindikire chirungamo chimenechi kapena ayi, ndi chirungamo chimene sichingakanidwe kapena kuzembeka kuti infa ikusendera chifupi nafe mofulumira. Ichi ndi chifukwa chake, zafotokozedwa mu Sūrah Al-Inshiqāq, Vesi 6:

يَا أَيُّهَا الْإِنْسَانُ إِنَّكَ كَادِحٌ إِلَىٰ رَبِّكَ كَدًّا فَلَقِيهِ ۖ

*E Iwe munthu, Ndithudi iwe ukubwerera kwa Mbuye wako,
kubwerera kotsimikizika ndipo uzakumana naye Iye.*

*[Kanz-ul-Īmān (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 30, Sūrah Al-Inshiqāq,
Vesi 6)*

Infā imabwera mozizimutsa

E inu amene mumawononga nthawi yofunikira pa zinthu zopanda pake! Talingalirani momwe moyo ukuthamangira mofulumira! Mwakhala mukuwona nthawi zambiri kuti yemwe anali kuwoneka wa thanzi komanso mphanvu watisiya modzidzimutsa. Ndipo sitimadziwa kuti chamuchitikira ndi chani komanso akukumana ndi zotani m'manda mwake. Komabe, iye akuyenera kunvesetsa chowonadi cha moyo.

E iwe amene mukuzikundikira chuma cha dziko lino! E iwe amene umakutenga kuzisonkhanitsira chuma ngati cholinga chokhacho cha moyo! Fulumirani! Kukonzekera tsiku Lomaliza kuwopera kuti mungakwiriridwe m'manda amdima m'mawa ngakhale mutagona bwino usiku. Chifukwa cha Allah عَزَّوَجَلَّ! Dzukani ku tulo ta kusalabadira. Allah عَزَّوَجَلَّ wanena m'vesi yoyamba ya Sūrah Al-Anbiyā kuti:

اِقْتَرَبَ لِلنَّاسِ حِسَابُهُمْ وَهُمْ فِي غَفْلَةٍ مُّعْرِضُونَ ﴿١٧﴾

Chiwerengero chayandikira kwa anthu, Pomwe iwo ali mukusalabadira komanso kunyozera.

[Kanz-ul-Īmān (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 17, Sūrah Al-Anbiyā, Vesi 1)

Kunong'oneza bondo ngakhale kwa okhala ku

Mwamba!

Okondedwa abale achisilamu! Ndikofunikira kwa ife kuti tizikumbukira ndikulingalira bwino za kagwiritsidwe bwino ntchito ka nthawi yathu. Kugwiritsa ntchito nthawi yathu mu zinthu zosapindulitsa kwa Mbuye wathu ndikuluza kwakukulu momwenso Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wanenera, 'Anthu kumwamba sazanong'oneza ndikukukuta mano kuzizuzula pa chilichonse ayi pamene anali pano pa dziko la pansi kupatula momwe anali kugwiritsa ntchito nthawi muzinthu zosakhala kupanga Żikr za Allah عَزَّوَجَلَّ.'

(Al-Mu'jam-ul-Kabīr, vol. 20, pp. 93-94, Ḥadīṣ 172)

Cholembela cha Nib

Hāfiẓ Ibn ‘Asākir walembe mu buku lotchedwa *Tabyīn-u-Kaẓib-il-Muftarī*: Pamene cholembela cha Sayyidunā Salīm Rāzī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ (munthu wolungama wa m'bado wachisanu) anali kuvala, iyenso رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anali kusongola cholembelachi akupanga ma Ẓikr kwa Allah عَزَّوَجَلَّ ndi cholinga choti asagwiritse ntchito nthawi yake mukusongola cholembela chokha ayi. (Ngakhale amachita zonsezi ku chinthu chothandizira kulemba ntchito ya chisilamu ndipo kutero kokha kuli ndi ubwino wochulukira, chimodzimodzi kupha mbalame ziwiri ndi mwala umodzi) iye رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anatengeranso mwayi pakupeza zinthu ziwiri nthawi imodzi.

Zalani Mtengo mu Paradizo!

Kufunikira kwa nthawi kukuwonekeranso pamene tikupeza kuti munthu atha kuzala mitengo yekha mu Paradizo ngakhale mu mphindi imodzi, pamene tikukhala pano pa dziko la pansi. Njira yozalira mitengo mu Paradizo pamene tili pa dziko pompano ndi yophweketsetsa kwambiri monga momwe zanededwera mu Ḥadīṣ ya *Ibn Mājah*, ‘Ntengo udzadzalidwa ku Paradizo kwa yemwe wolankhula mawu awa motere: (1) إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ اللَّهُ أَكْبَرُ لَا (2) الْحَمْدُ لِلَّهِ (3) سُبْحَنَ اللَّهِ (4)

(*Sunan Ibn Mājah*, vol. 4, pp. 252, Ḥadīṣ 3807)

Ubwino wofunira zabwino Mtumiki (Ṣalāt-‘Alan-Nabī ﷺ)

Okondedwa abale achisilamu! Monga momwe mwanvera kuti ndikosavuta kuti munthu azale ntengo mu Paradizo. Ngati amodizi mwa mawu atsogola pa mwambawo atchulidwa, ntengo umodzi umazalidwa ndipo ngati onsewo atchulidwa ndiye kuti mitengo inayi yonse imazalidwa kwa munthuyo mu Paradizo. Tsopano mutha kuwona kufunikira kogwiritsa ntchito bwino nthawi; mitengo itha kuzalidwa kwa ifeyo mu Paradizo pongogwedeza pang'ono lilime lathu kunena mawuwa.

Tikanakhala kuti tikuzala mitengo yathu yochuluka kwambiri mu Paradizo powerenga ‘سُبْحَنَ اللَّهِ سُبْحَنَ اللَّهِ’ m'malo mowononga nthawi yathu polankhula kapena kukambirana zosalungama! Kaya titayima, kuyenda, kukhala, kugona kapena kugwira ntchito, tiziyesetsa Kuwerenga Ṣalāt-‘Alan-Nabī mowirikiza, chifukwa muli ubwino wochuluka koposa mukutero. Wokondedwa komanso Wodalitsika Mtumiki ﷺ walankhula kuti, ‘Munthu yemwe angawerenge Ṣalāt kwa ineyo kamodzi, Allah عَزَّوَجَلَّ amampatsa zabwino zokwana khumi, amamuchotsera zolakwa zake khumi komanso amamukwezera ulemelero wake kokwana ka khumi.’ (*Sunan Nasāī, p. 222, Ḥadīṣ 1294*)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Kumbukirani! Pamene mukuwerenga chilichonse nthawi imene muli chigonere, mukuyenera kupinda miyendo yanu.

Okondedwa abale achisilamu! Tikanakhala kuti tinali ndi chizolowezi ndi ntima woyeza mawu athu tisanalankhule munjira iliyonse: Ngati chinthu chimene akufuna kulankhula chili ndi ubwino ku umoyo uno okha kapena umoyo uli nkunzanso. Ngati zingapezeke kuti mawu ake ndi osalungama, tikuyenera Kuwerenga Ṣalāt-‘Alan-Nabī kapena kuyamba kupanga Żikr za Allah عَزَّوَجَلَّ kusiyanana ndi kulankhula zinthu zosalungama ndikupeza ubwino ochuluka. Kapena tikuyenera kunena kuti: ‘سُبْحَنَ اللَّهِ’ kapena ‘الْحَمْدُ لِلَّهِ’ kapena ‘لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ’ kapena ‘اللَّهُ أَكْبَرُ’ kuti mitengo izalidwenso yochuluka mu Paradizo.

Kuposa zaka makumi asanu ndi chimodzi zopembeza

Ngati simukufuna Kuwerenga kalikonse, mungakhale mukupezabe zabwino mukukhala chete kwanu. Kusiyanana ndikumaganiza zolankhula mawu osalungama pa dziko pano, mukumbukireni Allah عَزَّوَجَلَّ komanso Wokondedwa Rasūl صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ mu malingaliro chabe kapena mukuchita pa Maphunziro a Chisilamu kapena zowawa za infa, kusungulumwa ndi kuwopsa kwa manda ndi kuwopsa kwa tsiku lachiweruzo. Munjira imeneyi, nthawi yanu siyizawonongeka ndipo mpweya uliwonse mungatulutse mukupuma إِنَّ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ uzatengedwa ngati kupembeza.

Zanenedwa mu *Al-Jāmi'-uṣ-Ṣaghīr* kuti Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ walankhula kuti, 'Kulingalira (za tsiku lomaliza) kwa mphindi ngakhale imodzi ndikopambana kwambiri kuposa kupembeza kwa zaka makumi asanu ndi chimodzi.' (*Al-Jāmi'-uṣ-Ṣaghīr*, p. 365, Ḥadīṣ 5897)

Zinthu zomwe tikuyenera kuchita zinthu zisanu zisanafike

Okondedwa abale achisilamu! Mosakayika, moyo ndi wawufupi. Ndipo tinene kuti, nthawi tili nayo ndi yokhayo yomwe tili nayo m'manja mwathu. Chikhulupiriro chilichonse choti nthawi tili nayo mtsogolomu ndi chabe koma chinyengo. Pali kuthekera kwakukulu kuti titha kukumana ndi infa mu mphindi ikubwerayi. Rasūlullāh صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ walankhula kuti:

إِغْتَنِمْ خَمْسًا قَبْلَ خَمْسٍ: شَبَابَكَ قَبْلَ هَرَمِكَ وَصِحَّتَكَ قَبْلَ سَقَمِكَ
وَعِثَاكَ قَبْلَ فَقْرِكَ وَفَرَاغَكَ قَبْلَ شُغْلِكَ وَحَيَاتَكَ قَبْلَ مَوْتِكَ

Kumasulira: Zisamalen zinthu zisanu (ntchito) zisanafike zinthu zisanu (1) chinyamata usanafike ukalamba, (2) thanzi lanu musanadwale, (3) chuma chanu musanasawuke, (4) nthawi yanu yopuma yotanganidwa isanafike, (5) kukhala wamoyo infa isanabwere (*Al-Mustadrak*, vol. 5, pp. 435, Ḥadīṣ 7916)

Kukonderedwa kuwiri

Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ walankhula kuti, 'Pali

zinthu zimene anthu anakonderedwa zomwe iwo samazindikira za chimenechi. Chinthu choyamba ndi thanzi lathu komanso nthawi yathu yopuma.’

(*Ṣaḥīḥ Bukhārī*, vol. 4, pp. 222, Ḥadīṣ 6412)

Okondedwa abale achisilamu! Mosakayika, munthu wodwala athanso kunvesetsa kufunikira kwa moyo kuyerekeza ndi yemwe thupi lake lili la thanzi. Chimodzimodzi, munthu wotanganidwa ndi amene angazindikire kufunikira kwa nthawi. Anthu onse amene samakhala otanganidwa kawiri kawiri ndi amene samazindikira kufunikira kwa nthawi. Igwiritseni nthawi yanu ndipo yigwiritseni bwino ntchito munjira iliyonse mungakwanitse kupewela kulankhula mawu osalungama, kutenga nawo gawo mu zochitika zosalungama komanso kukhala pa ubwenzi ndi anzanu ochita chosalungama.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Ubwino wa Chisilamu

Zinalankhulidwa mu Sunan-ut-Tirmizī: Yemwe anatumizidwa kukhala chisoni ku zolengedwa zonse, yemwe ndi Wolemekezeka Mtumiki صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ walankhula kuti, ‘Kusiya chomwe chili chosathandiza kwa munthu ndi umodzi mwa mitendere imene iye anapeza chifukwa cha Chisilamu.’

(*Sunan-ut-Tirmizī*, vol. 4, pp. 142, Ḥadīṣ 2344)

Kufunikira kwa nthawi

Okondedwa abale achisilamu! Umoyo uli ndi masiku owerengeka, mawola komanso mphindi. Mpweya uliwonse tikupumawu ndi golide wantengo wapatali. Tikanakhala kuti tikuwerengera kufunikira kwa mpweya uli wonse tikanawugwiritsa ntchito mukupanga ntchito zabwino! Ngati tingayiwononge nthawi yanthu mukulankhula komanso kuchita ntchito za uchimo tizalira mogwesa msozi ya kunong'oneza bondo komanso kukhumudwa pa Tsiku lachiweruzo pambuyo pozawonesedwa kawundula wa ntchito zathu ndikupeza lopanda kalikonse kabwino. Tikanakhala kuti timalingalira momwe nthawi ya moyo wathu tikuyigwiritsira ntchito tikanakhala tikuganizira za chimenechi. Tiyenera kuyetsetsa kugwiritsa ntchito nthawi yathu mu ntchito yokhayo yopindulitsa kuti tipewe kuwononga nthawi mukulankhula komanso kugwiritsa ntchito popanga kaduka komanso mijedo. Kupanda apo, tizakhala odandawula kwambiri Tsiku lachiweruzo.

Mawu a anthu amene anayigwiritsa bwino ntchito nthawi

- ❖ Amīr-ul-Muminīn, Sayyidunā ‘Alī كَرَّمَ اللَّهُ وَجْهَهُ الْكَرِيمُ walankhula kuti, ‘Masiku athuwa ali ngati matsamba a moyo wathu, akongoletseni matsamba anu ndi ntchito zabwino.’

- ❖ Sayyidunā ‘Abdullāh Ibn Mas’ūd رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ walankhula, ‘Ndimakhala okhumudwa komanso wamanyazi pa tsiku limene sindinachite ndikuchulukitsa ntchito zanga zabwino.’
- ❖ Sayyidunā ‘Umar Bin ‘Abdul ‘Azīz رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ walankhula kuti, ‘Umoyo wanu ukuchepera chepera tsiku ndi tsiku, ndiye chifukwa chani mukupanga ulesi kugwira ntchito zabwino?’ Munthu wina anati mozichepetsa kwa iye, ‘Yā Amīr-ul-Mu`minīn! Yimikani ntchitoyi mpaka mawa.’ Iye رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ anati, ‘Nthawi zambiri ndimavutika kumaliza ntchito yanga mu tsiku limodzi; ngati ndingayimike ntchito yanga mpaka mawa, ndiye nkotani kuti ndizakwanitse kumaliza ntchito ya masiku awiri mu tsiku limodzi?’
- ❖ Osayimika ntchito ya lero mpaka mawa, chifukwa uzakhala ndi ntchito ina mawalo.
- ❖ Sayyidunā Ḥasan Baṣrī رَحِمَهُ اللَّهُ عَلَيْهِ anafotozoza kuti, ‘E iwe munthu! Moyo wako wazaza ndi masiku. Pomwe masikuwa amakhala akudusa, gawo lina la moyo wako nalo limakhala likutha.’ (*Tabqāt-ul-Kubrā lil-Manāwī, vol. 1, pp. 259*)
- ❖ Sayyidunā Imām Shāfi’ī رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ walankhula kuti, ‘Ndakhala ndikuyenda ndi anthu olungama kwa nthawi yayitali, kupeza phindu la mu uzimu. Ndaphunzira zinthu zofunikira ziwiri mukukhala nawo anthuwa: (1) nthawi ili

ngati lupanga, ukuyenera kumadulira (ntchito zabwino) apo ayi izakudula iweyo (pokupanga iwe kukhala wokangalika ndi zinthu zosapindulitsa komanso zosafunikira) komanso (2) utetezeni ntima wanu; ngati siwukuwuyika mu kukangalika ndi ntchito zabwino, ntima uzakuyikani mukukangalika ndi zinthu zoyipa.’

- ❖ Imām Rāzī رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ anati, ‘Ndikulumbira mwa Allah عَزَّوَجَلَّ Ndimakhala wokhumudwa kwambiri pamene ndikudya chifukwa ndimayenera kusiya zichitochito za chipembezo (kulemba kapena Kuwerenga). Nthawi ndi chinthu chofunikira kwambiri.’
- ❖ Hāfiẓ Ibn Hajar رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ akufotokoza zokhuza Sayyidunā Shamsuddīn Aṣḥāhānī قُدِّسَ سِرُّهُ النَّوْزَانِي (munthu wophunzira kwambiri ziphunzitso za Imam Shāfi’ī mu m'bado wachisanu ndi chitatu (8): Iye رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ anali kudya pang'ono kuwopesera kuwonongeka kwa nthawi pakupita ku chimbuzi moworikiza.

(Ad-Dur-rul-Kāminah lil-‘Asqalānī, vol. 4, pp. 328)

- ❖ ‘Allāmah Ṣaḥbī رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ walembe mu buku lotchedwa Taḥkira-tul-Ḥuffāẓ zokhuza Khaṭīb-e-Baghdādī رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ: ‘Iye رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ anali Kuwerenga ngakhale iye akuyenda (ndi cholinga choti asawononge nthawi yomwe akuyenda kuchoka malo ena kupita ena). *(Taḥkira-tul-Ḥuffāẓ, vol. 3, pp. 224)*

- ❖ Sayyidunā Junayd Baghdādī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anali Kuwerenga buku Lolemekezeka la Quran mu nthawi yake yomwalira. Munthu anafunsa modabwitsika, ‘Kuwerenga ngakhale mu nyengo ino!’ Iye رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anayankha, ‘Buku langa lazabwino likutsekedwa, ndiye ndikuwonjezera ntchito zabwino mu bukuli mwansanga.’ (*Ṣīd-ul-Khāṭir li Ibn-ul-Jawzī*, pp. 227)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Khazikitsani chizolowezi

Okondedwa abale achisilamu! Ngati nkotheke, pangani ndikukhazikitsa chizolowezi chanu. Choyambirira, yesetsani kugona m'mawola awiri mukangopemphera Salāt-ul-‘Ishā. Macheza komanso miseche ndi anthu (zimene zilibe ubwino uliwonse wa chipembezo) usiku kukhalira kupita ndikupezeka m'malo ogona alendo ngati m'mahotela, m'makalabu ndi malo ena. kutero ndikuluza kwa kukulu. Zafotokozedwa mu *Tafsīr Rūḥ-ul-Bayān*, volumu 4, pa tsamba 166: ‘Chimodzi mwa zifukwa za kuwonongeka kwa anthu a m'neneri Lūt chinali kusunkhana kwawo mbali za mtsewu ndikumaseka komanso kuselewulana.’

Okondedwa abale achisilamu! Khalani wonjenjemera ndi mantha kwa Allah عَزَّوَجَلَّ! Posatengera mawonekedwe olungama a nzako, mukuyenera kupewa komanso kulapa za kupezeka

kwanu mu ubale omwe umakupangitsani kusalabadira za Allah عَزَّوَجَلَّ. Gonani mofulumira pomwe mwamaliza kugwira ntchito za chipembezo chifukwa kupuma kwanu usiku ndi kopambana kuyerekeza ndikupuma kwanu masana kuthupi komanso ku chibadidwe. Zalankhulidwa mu Sūrah Al-Qaṣaṣ, Vesi 73:

وَمِنْ رَحْمَتِهِ جَعَلَ لَكُمُ اللَّيْلَ وَالنَّهَارَ لِتَسْكُنُوا فِيهِ وَلِتَبْتَغُوا

مِنْ فَضْلِهِ وَتَعْلَمُوا تَشْكُرُونَ ﴿٧٣﴾

Ndipo mu chifundo Chake anakupangirani usiku ndi usana, kuti Muzipumulamo ndi Kufunafuna zabwino zake, ndi kuti mulandire chowonachi ndikukhala othokoza.

[Kanz-ul-Īmān (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 20, Sūrah Al-Qaṣaṣ, Vesi 73)

Kuyikira ndemanga pa Vesi lawerengedwali, Ḥakīm-ul-Ummat Muftī Aḥmad Yār Khān رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ walembe pa tsamba 629 la Nūr-ul-‘Irfān, ‘Vesi limeneli likutitsimikizira kuti kupuma usiku ndikumatakataka usana pa moyo wathu ndi zopambana. Osakhala maso usiku wonse popanda chifukwa choyenera, kapena kugwiritsa ntchito usana wathu mukupanga zinthu zosalungama. Komabe, ngati munthu wagona masana ndikumagwira ntchito usiku chifukwa cha mtundu wa ntchito yake, palibe chovuta mukutero.’

Kupambana kwa m'mawa

Ndikofunikira kwambiri kulingalira komanso kukhala chidwi

ndi ntundu wa ntchito imene tikugwira pokhazikitsa m'ndandanda momwe tizigwirira ntchito komanso kupembeza. Mwachitsanzo, Msilamu yemwe amagona usiku amakhala wopepukidwa thupi lake pafupifupi mamawa uliwonse. Pachifukwachi, ku m'mawa ndi nthawi yabwino kupanga maphunziro. Du'ā yotsatirayi ya Rasūlullāh ﷺ yakambidwa mu buku la *Sunan-ut-Tirmizī*: 'Yā Allah ﷻ chulukitsani madalitso am'mawa ku Ummaḥ wanga.'

(Sunan-ut-Tirmizī, vol. 3, pp. 6, Ḥadīṣ 1216)

Poyikira ndemanga zokhuza Ḥadīṣ, Muftī Aḥmad Yār Khān رحمه الله عليه walankhula kuti, 'Kumeneko ndikunena kuti, (E inu Mbuye wanga Allah ﷻ) chulukitsani madalitso mamawa uliwonse mu maphunziro onse achipembezo komanso adziko lapansi kuchokera mu zomwe Ummaḥ wanga umachita nthawi yaku m'mawa. (chitsanzo, pa ulendo opeza maphunziro, komanso malonda, mwazina.).'

(Mirāt-ul Manājīḥ, vol. 5, pp. 491)

Yesetsani kuganiza ndikulingalira bwino lomwe za m'mene mumagwiritsira ntchito tsiku ndi tsiku kuyambira pomwe dzuwa latuluka ku m'mawa kufikiranso usiku. Mwachitsanzo, Taḥajjud mu nthawi yakuti yakuti, kuphunzira maphunziro achipembezo, kupemphera Ṣalāt-ul-Fajr pa Jamā'at (komanso Ṣalāḥ zina zonse) mu Masjid ndi Takbīr yoyamba, Ishrāq, Chāsht, kudya kapena kumwa kadzutsa, Kupeza zinthu

munjira ya Ḥalāl, kudya nkhomaliro, kugwira ntchito za pakhomo, kugwira ntchito za madzulo, kukhala ndi kupezeka anzanu abwino (ngati kutero ndikosatheka, ndiye kuti kucheza nokha ndi kwabwino koposa), kukumana ndi abale achisilamu ndi zolinga za chipembezo, mwazina.

Zinthu zonsezi zizigwirika ndi kuyendesedwa mu nthawi yoyenera. Anthu ambiri atha kumakumana ndi mavuto poyambirira, koma pang'ono pang'ono lizakhala khalidwe lawo ndipo azawona m'dalitso wake, *إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ*.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Okondedwa abale achisilamu! Pamene tikumaliza mawuwa, Ndikufuna nditatchula ubwino wa Sunnaḥ komanso ma Sunan ndi zikhalidwe zabwino. Mtumiki wa Raḥmaḥ, muwomboli wa Ummaḥ *صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ* walankhula, ‘Yense wokonda ma Sunnaḥ anga wandikonda ine ndipo yemwe wandikonda ine azakhala nane ku Paradizo.’

(Mishkāṭ-ul-Maṣābīḥ, vol. 1, pp. 55, Ḥadīṣ 175)

Ngale 15 za luntha pogona komanso kudzuka

- ❖ Sasani Fumbi pa Kama lanu musanayambe kugwiritsa ntchito ndi cholinga chofuna kuchotsa zilombo ndi zina zotero., ngati ziripo.

- ❖ Werengani Du'ā iyi musanagone:

اللَّهُمَّ بِاسْمِكَ أَمُوتُ وَأَحْيَا

- Kumasulira:** E Allah عَزَّوَجَلَّ m'dzina lanu Ndikumwalira komanso kukhala ndimoyo (mwachitsanzo kugona komanso kudzuka). (*Ṣaḥīḥ Bukhārī, vol. 4, pp. 196, Ḥadīṣ 6325*)
- ❖ Osagona pambuyo pa Ṣalāt-ul-‘Aṣr chifukwa chitha kukhala chifukwa chakusagwira bwino kwa ubongo wanu. Rasūlullāh صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, ‘Yense wosakhala ndi nzeru chifukwa cha kugona pambuyo pa Ṣalāt-ul-‘Aṣr akuyenera kuzikonza yekha basi.’ (*Musnad Abī Ya’lā, vol. 4, pp. 278, Ḥadīṣ 4897*)
 - ❖ Kugona pang’ono masana ndi Mustahab. (*Fatāwā ‘Ālamgīrī, vol. 5, pp. 376*) Ṣadr-ush-Sharī’ah, Badr-ut-Tarīqah ‘Allāmah Maulānā Muftī Muhammad Amjad ‘Alī A’zamī رَحِمَهُ اللهُ عَلَيْهِ walankhula kuti, ‘Kutero ndi kotheka kwambiri kwa amene achezera usiku kupemphera Ṣalāh, kupanga ma Ṣikr a Allah عَزَّوَجَلَّ kapena kukangalika muKuwerenga. Qayirura imachotsa kutopa kumene kumabwera chifukwa cha kuchezera.’ (*Bahār-e-Sharī’at, gawo16, pp. 79*)
 - ❖ Ndi Makrūh kugona kumayambiriro kwa tsiku kapena pa katikati pa Maghrib ndi ‘Ishā. (*Fatāwā ‘Ālamgīrī, vol. 5, pp. 376*)
 - ❖ Ndi zokondedwa (Mustahab) kugona pomwe tili woyera.

- ❖ Ndi zokondedwa (Mustahab) kugonera m'mbali ya kumanja mosamira nkono wanu wa manja ndi dzanja lanu la manja mosamirisira tsaya lanu lakumanja molunjika ku Qiblaḥ kwa kanthawi ndikutembenukira mbali ya manzere. (*Fatāwā 'Ālamgīrī, vol. 5, pp. 376*)
- ❖ Pomwe mukupita kokagona, lingalirani mukugona 'kuti mwagona' m'manda m'mene mulibe aliyense ngati nzanu kupatula ntchito zanu.
- ❖ Pamene mukugona, kangalikani nokha mukuchita ma Žikr a Allah عَزَّوَجَلَّ (mwachitsanzo: pitirizani kunena mawuwa, 'سُبْحَنَ اللَّهِ', 'الْحَمْدُ لِلَّهِ', لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ) (mpakana tulo litakutengani chifukwa munthu azazutsidwa mu nyengo imene anagonera ndipo azaweruzidwa pa Tsiku lachiweruzo momwenso iye anafera. (*Fatāwā 'Ālamgīrī, vol. 5, pp. 376*))
- ❖ Pambuyo poti mwadzuka, werengani Du'ā iyi:

الْحَمْدُ لِلَّهِ الَّذِي أَحْيَانَا بَعْدَ مَا أَمَاتَنَا وَإِلَيْهِ النُّشُورُ

Kumasulira: Kutamandidwa konse ndikwa Allah عَزَّوَجَلَّ
Yemwe watipatsa moyo pambuyo potipatsa infa ndipo kwa Iye tizabwerera.

(*Ṣaḥīḥ Bukhārī, vol. 4, pp. 196, Ḥadīṣ 6325*)

- ❖ Pambuyo podzuka, tsimikizani mwa tunthu kufuna kusintha ndikukhala wa mantha komanso kupewa kukhala chiphinjo kwa ena.

(Fatāwā ‘Ālamgīrī, vol. 5, pp. 376)

- ❖ Pomwe mwana wa mwamuna komanso wa nkazi wafika zaka khumi zakubadwa (10), akuyenera kusiyantsidwa pogona ndikugona pa kama zosiyana. Mwana wa mwamuna yemwe wafika nsinkhuwu sakuyenera kugona malo amodzi ndi anzake kapena azibambo pa kama imodzi.

(Durr-e-Mukhtār, vol. 9, pp. 629)

- ❖ Pamene Bambo komanso mayi agona pa kama limodzi, sakuyenera kumulora mwana wa zaka khumi zakubadwa kugona naye malo amodzi ndi iwo. Pamene m'nyamata wafika potha nsinkhu, malamulo a abambo azakhazikitsidwa ndikugwira ntchito pa iye. *(Durr-e-Mukhtār, vol. 9, pp. 630)*

- ❖ Gwiritsani ntchito Miswāk (potsukira mano anu) pamene mwadzuka.
- ❖ Kudzukira usiku kuti mupemphere Taḥajjud ndi ntchito yopambana kwambiri. Mtumiki Wokondedwa ndi Wodalitsika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ walankhula kuti, ‘Farḍ Ṣalāh,

Mwala Wantengo Wapatali (Dayamondi)

zikatha zimasala ndi Ṣalāḥ zimene zimapempheredwa mukufuna kwa munthu usiku.’

(Ṣaḥīḥ Muslim, pp. 591, Ḥadīṣ 1163)

Phunzirani ma Sunan, gulani ka buku komwe mutu wake ndi ‘Sunnatayn aur Ādāb’ (ma Sunan komanso Miyambo) kuchokera ku Maktaba-tul-Madīnaḥ. Yendani pamodzi ndi ma Madanī Qāfilaḥ a Dawat-e-Islami limodzi ndi omukonda Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ chifukwa kutero ndi njiranso yabwino kwambiri ndikumuthandizira munthu kuphunzira komanso kuchita ma Sunnaḥ.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Tchati cha Kunvetsetsa Malemba

ء	A/a	ژ	Ř/ř	ل	L/l
ا	A/a	ز	Z/z	م	M/m
ب	B/b	ژ	X/x	ن	N/n
پ	P/p	س	S/s	و	V/v,
ت	T/t	ش	Sh/sh		W/w
ٹ	Ṭ/ṭ	ص	Ṣ/ṣ	ه / ه / ة	Ĥ/ĥ
ث	Ṣ/ṣ	ض	Ḍ/ḍ	ی	Y/y
ج	J/j	ط	Ṭ/ṭ	ے	Y/y
چ	Ch	ظ	Ẓ/ẓ	َ	A/a
ح	H/h	ع	‘	ُ	U/u
خ	Kh/kh	غ	Gh/gh	ِ	I/i
د	D/d	ف	F/f	و مدّہ	Ū/ū
ڈ	Ḍ/ḍ	ق	Q/q	ی مدّہ	Ī/ī
ذ	Ẓ/ẓ	ك	K/k	ا مدّہ	Ā/ā
ر	R/r	گ	G/g		

Kuti Mukhale Msilamu Wopembedza
Komanso Wosunga Swala

Muzikhala usiku wonse mu Ijtima' yolimbikitsa Sunnah ya pa Sabata ya Dawat-e-Islami, yomwe imachitika Lachinayi lililonse pambuyo pa Swala ya Maghrib mu mzinda wanu, kuti mukondweretse Allah ﷻ ndi zolinga zabwino. Pofuna kuphunzira ma Sunnah, chikhale chizolowezi chanu kuyenda ulendo wa masiku atatu wa Madani Qafilah mwezi uliwonse pamodzi ndi okonda Mtumiki (Rasul), lembani nkabuku ka Madani In'amat tsiku lililonse pochita Fikr-e-Madinah, ndipo muzikapereka kwa m'bale wachisilamu woyenerera wa m'dera lanu pa tsiku loyamba la mwezi uliwonse wa Madani.

Cholinga Changa cha Madani: 'Ndiyesetsa kudzisinthana ndekha ndi anthu a dziko lonse lapansi, *إن شاء الله عز وجل*.' Kuti tidzisinthe tokha, tiyenera kutsatira Madani In'amat ndipo poyesetsa kusintha anthu a dziko lonse lapansi, tiyenera kuyenda ndi ma Madani Qafilah, *إن شاء الله عز وجل*.



ISBN 978-969-631-524-7



0109558



MC 1286

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagaran
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan.

UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 1262

Web: www.dawateislami.net | E-mail: translation@dawateislami.net